Ndondomeko Yoyhandiza Alimi

(The Farmer Input Support Programme)

Anthu ambili a mbali za kumidzi mu Zambia amadalira pa ulimi. Ambiri a iwo ndi osauka kwambiri motero kuti amagulanso cimanga cakudya ngakhale kuti iwonso ndi alimi a cimanga. Boma liri ndi zigawo zitatu zaulimi – cigawo coona pa zakudya (the Food Security Pack Programme), cigawo coona pa kasungidwe ndi kugula zolimidwa (the Food Reserve Agency [FRA]), ndi cigawo coona pa zipangizo zothandizila alimi pa ulimi wao (the Farmer Input Support Programme [FISP], cimene kale cinkapereka feteleza kwa alimi).

Cigawo ca FISP cimapereka kwa alimi woyenerera thandizo la zofunikira la 80 pelesenti (80%) ya feteleza komanso 50 pelesenti (50%) ya mbeu kulingana pa muyeso wa hekitala limodzi la cimanga. Atsogoleri a m'madera omweo ndi amene amasankha alimi woyenerera thandizo limeneli, ndipo wosankhidwa ayenera kukhala:

- atalembetsa maina ao ku gulu la alimi;
- alimi a cimanga, olima pakati pa hekitala limodzi ndi mahekitala asanu; ndipo
- okwaniritsa kulipira ngongole yokhalira ya zinthu zimene anagula.

Alimi ayeneranso kulipiliratu ndalama ya zipangizo, zimene zimabweretsedwa ndi makampani osankhidwa pambuyo pake kupyolera mwa anchito a zamtengatenga komanso azamalonda aulimi.

african centre for biodiversity

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156